

CHIKRISTU NDI CHISALAMU

Pakuti mtundu ndi ufumu umene udzakana kutumikira udzaonongeka, inde mitundu imeneyo idzasakazidwa ndithu" Yesaya 60:12. Paciyam, bi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi Genesis 1:1 ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'chifanizo chathu. Monga mwa chikhalidwe chathu: Genesis 1:26 Lero pa dziko lonse lapansi maiko ambiri adalandira ufulu odzilamurila, komankhondo imene yasautsa anthu ambiri ndi kudziwa Mulungu woona amene ayenela kumukhulupirila ndi kumulambira. Mulungu wolenga kumwamba ndi dziko lapansi anati ***"usakhale nayo milungu ina koma ine ndekha"***

Eksodo 20:3.

CHISALAMU

Chislamu ndi chipembedzo chokhala ndi m'tsogoleri wake, malamulo ake ndi miyambo yakenso. M'tsogoleri wa Chislamu ndi munthu amene adamwalira dzina lake Muhammod .

Muhammod anabadwa m'chaka cha 570 AD, anayamba nchito yake monga m'neneri m'chaka cha 613 AD, ndipo anamwalira mchaka cha 632 AD. Chislamu chili ndi mizati imnene chiyadzamilapo. Olemba buku lochedwa **"Understanding Islam"** anati mizatiyi ilipo isanu, koma olemba **"Slavery, Terrorism and Islam"** Dr. Peter Hammond anati Pali mizatu isanu ndi umodzi (6) nati anthuwa anati mizati ya chipembezo chawo ndi 5, chifukwa wa 6 ndi nkhondo imene anaicha "nkhondo yoyera" Jihad.

Koma inayi ndi iyi:

1. Shahada - Kuvomereza poyera chikhulupiriro chawo.
2. Sawn - Kusala kudya mwezi wa Ramadan onse, atadya madzulo, mpaka m'wama.
3. Salah - Kupemphera kasanu pa tsiku limodzi.
4. Zakah - Kupatsa chaufulu kwa ena (koma molengeza).

5. Hajj - Ulendo wa ku Mecca ngakhale kamodzi mu umoyo onse.

Ma muslimu amakhulupirira pa zinthu 5 kuti avomerezeke kukhala m'modzi wa iwo.


1. Mulungu umodzi (allah).
2. Angelo alipodi.
3. Mabuku onse ovumbulutsidwa asanu olembedwa ndi Moses, Salimo la David, chipangano chatsopano ndi Quran.
4. Aneneri otumidwa ndi Mulungu pakati pawo pali Muhammod ndi Yesu.
5. Kuuka kwa a kufa, kumene kuphatikiza ulosi wa Tsiku Lomariza la chiweruzo kumene adzaonetsa kopita, m'silamu, ku Gehena kapena ku paradiso.

CHIKHRISTU

Chikristu ndi moyo umene umapezeka mwa m'tsogoleri amene anati ine ndine kuuka ndi moyo yense okhulupirira ine angakhale amwalira adzakhala ndi moyo" Yohane 11:25 - 26.

Zipembedzo zili ndi kumene zalinga, zili paulendo opita kumapeto, ulendo ulionse uli ndi njira yake. Mtsogoreli wa Chikristu Yesu anati: mapeto a Chikristu ndi moyo wosatha, ndipo kuti munthu akafike ku moyo wosatha, mjira yake ndi Yohane 14:6. Chikristu si chipembedzo chabe koma moyo. Akristu Buku lawo ndi Baibulo mau ake a Mulungu . Asilamu Buku lawo ndi Quran imene anati Muhammod adalandila kwa m'ngelo Gabriel.

Pamene mukuwerenga pepala iyi, dziwani kuti mwapatsidwa mwayi osankha chimene muyenela kutsatira, chifukwa tsiku lina mwayi umenewu udzakhala utakutherani. Mudzaufuna koma sudzapezeka. Lero ngati inu mukhulupirira Ambuye Yesu mudzapulumuka. Machitidwe 16:31 pakuti palibe dzina lina limene tingapulumsidwe nalo Machitidwe 4:12 kuti mudziwe zambiri, kapena muli ndi funso lembelani ku keyala iyi.



CHIKRISTU

CHIKRISTU NDI CHISLAMU



CHISALAMU

<u>Quran</u>	<u>Baibulo</u>
Buku limodzi	Mabuku 66
Wolembe mnthu umodzi	Wolembe anthu 40
Chilankhulidwe chimodzi	Zilankhulo 3
Dziko limodzi	Makontinenti 3
Lolembedwa mu zaka23	Lombedwa mu zaka 1500
Mulibe Ulosi	Muli Ulosi
Mulibe Zodabwitsa	Muli Zodabwitsa
Manda ku Medina	Manda apululu ku Yerusalemu
Mulibe Chiwombolo	Muli Chiwombolo
Muli adani pa adani	Chikondi pa adani
Muli ukapapolo	Muli Ufulu



Frontline Fellowship
P.O. Box 74 Newlands
7725
Cape Town South Africa
Tel: (+27) 21-689-4480
mission@frontline.org.za
www.frontline.org.za

